STANDARD 4 SOCIAL STUDIES SUMMARY NOTES

COMPILED BY BLESSINGS NKHOMA

A TEACHER AT KASACHE PRIMARY SCHOOL

THAVITE ZONE

SALIMA DISTRICT

0998603292/0881845347

CHICHEWA VERSION

MUTU 1: NTCHITO ZA MFUMU YAMPANDO

Dera la mfumu yampando

-Dera la mfumu yampando litha kudziwika pogwritsa ntchito mbali za dziko monga kumpoto, kumwera, kuvuma ndi kuzambwe kapena zinthu zina zozungulira delari.

-Zinthu zina zozungulira dera zikhoza kukhala zachilengedwe kapena ma dera a mafumu a mipando ina.

Atsogoleri m'dera la mfumu yampando


-Dera la mfumu yampando ndi dera lalikulu.

-Derali limakhala ndi midzi yambiri.

-Mudzi uliwonse umayang'aniridwa ndi nyakwawa.

-Midzi ingapo amayang'anira ndi gulupu.

Ndondomeko yosonyeza dera la mfumu yampando



●Chifukwa cha kukula Kwa derali, atsogoleri amakhala ambiri. Atsogoleri opezeka m'dera la mfumu yampando ndi monga gulupu, nyakwawa ndiponso khansala.

Ntchito za mfumu yampando

-Kuweruza milandu

-Kulimbikitsa anthu awo pa ntchito za chitukuko.

-Kuonetsetsa kuti anthu awo akusunga bata ndi mtendere.

MUTU 2: ATSOGOLERI NDI CHITUKUKO M'DERA LA MFUMU YAMPANDO

Chitukuko

-Chitukuko ndi chofunika m'dera lililonse. Ndi udindo wa atsogoleri kubweretsa chitukuko.

Udindo wa atsogoleri pachitukuko

-Amayambitsa chitukuko

-Amalimbikitsa anthu awo kuchita chitukuko.

Chifukwa chimene anthu amalemekezana

-Amafuna ena awalemekeze.

-Amafuna dera lawo likhale ndi mbiri yabwino.

Chifukwa chimene atsogoleri amalemekezedwa

-Chifukwa cha udindo wawo ngati atsogoleri.

Zomwe anthu amachita polemekeza atsogoleri

-Kuwamvera

-Kuwagwadira

MUTU 3: MGWIRIZANO M'DERA LA MFUMU YAMPANDO

Nthawi yomwe mgwirizano umafunika

●Nthawi ya chisangalalo monga zikwati, mapemphero, magule amakolo athu, masewero ndi pamiyambo yosiyanasiyana ya chikhalidwe chathu.

●Nthawi ya chisoni monga pamatenda, maliro komanso nthawi yamavuto ogwa mwadzidzidzi.

●Nthawi yogwira ntchito zachitukuko m'madera athu monga kuumba njerwa, kumanga milatho ndi kulambula misewu ya m'madera athu.

Kufunika kwa mgwirizano

●Umalimbikitsa kusunga ndi kupititsa patsogolo chikhalidwe chathu.

●Umalimbikitsa umodzi.

●Umalimbikitsa kudalirana.

●Umalimbikitsa kudzipereka pokweza dziko lathu.

MUTU 4: ZACHILENGEDWE ZA M'DERA LA MFUMU YAMPANDO

Zachilengedwe zopezeka mdera la mfumu yampando

-Mitsinje

-Mapiri

-Zidikha

-Zigwa

-Nyanja

Ubwino wa zinthu zachilengedwe

●Nthaka yabwino ya muzidikha ndi zigwa imathandiza pa ntchito ya ulimi.

●Madzi ochokera m'mitsinje ndi nyanja amagwiritsira ntchito pakumwa, kuphikira, kuchapira ndi kuthirira mbeu.

●Nsomba zimagwiritsidwa ntchito ngati ndiwo.

●Mitengo imagwiritsidwa ntchito ngati milimo komanso matabwa.

●Zidikha ndi zigwa ndi malo amene miseu ndi njanji zimamangidwa mosavuta.

Mmene anthu amaonongera zachilengedwe

-Kudula mitengo mwachisawawa

-Kumweta udzu wopezeka m'mapiri mwachisawawa.

-Kubutsa moto wolusa ndi kuwotcha tchire lonse kotero nthaka imakhala yosatetezedwa ndipo imakokololedwa ndi madzi ndi mphepo yamkuntho.

Njira zosamalira zachilengedwe

-Kubzalanso mtengo m'mapiri, muzigwa ndi muzidikha pobwezeretsa mitengo yomwe yadulidwa.

-Kupewa kuyatsa tchire.

Kufunika kwa zachilengedwe zopezeka m'dera la mfumu yampando

CHILENGEDWE	ZINTHU ZOPEZEKAMO	NTCHITO YAKE
Mapiri	Mitengo, udzudzu ndi miyala	-Kumangira nyumba -Kukonzera miseu
Zidikha	Nthaka yabwino	-Kulima -Kulima miseu ndi kukonza njanji -Kumanga nyumba
Mitsinje	-Madzi -Bango -Nsomba	-Kumwa -Kumangira -Kudya
Nyanja	-Nsomba	-Kudya

	-Madzi	-Kumwa -Kusamba
Zigwa	Nthaka yabwino	-Kulima

MUTU 5: NYENGO

Kaonekedwe ka nyengo

a) Nyengo yadzinja

-Iyi ndi nyengo imene mvula imagwa ndipo kumamera zomera zambiri. Tizirombo tambiri timauluka. Iti ndi tizilombo ngati abongololo, nkhululu, abololo ndi inswa.

b) Nyengo yachilimwe

-Iyi ndi nyengo yotentha. Mitengo imayamba kuphukira masamba, msipu umasowa. Alimi amayamba kukonza kumunda kukonzekera nyengo ya mvula.

c) Nyengo yachisanu

-Iyi ndi nyengo yozizira. Mitengo imayoyola masamba. Mbalame ndi tizilombo tina timasowa.

Mmene kusintha kwa nyengo kumakhudzira miyoyo

●Zizindikiro za mmene kwachera zimasintha ndi mmene nyengo ilili.

●Nthawi yachilimwe, madzi amasowa ndipo anthu amakatunga madzi kutali.

●Nthawi yadzinja madzi amakhala ambiri ndipo m'madera ena amasefukira, komanso zakudya zimakhala zambiri.

●Zakudya zimasintha malinga ndi nyengo.

●Nthawi yachilimwe udzu wodyetsa ziweto umasowa.

●Ntchito zina zimatha kulephereka malingana ndi mmene nyengo ilili.

MUTU 6: KUSAMALA MADZI

Malo amene tingapezeko madzi

-M’mitsinje

-Mnyanja

-Makhwawa

-M’madambo

Njira zogwiritsira ntchito madzi m’dera

-Kumwa

-Kuthirira mbewu

-Kuphikira

-Kuchapira

Njira zimene zimaononga madzi

-Kuchapa m’mitsinje.

-Kukodzera m’madzi.

-Kuchita chimbudzi m’madzi kapena kutchire,

-Kuthira mankhwala oipa m’madzi.

Matenda omwe amadza kamba komwa madzi oipa

-Kamwazi

-Kutsegula m’mimba

Njira zosamalira madzi

-Kuwiritsa madzi akumwa amene tatunga ku mtsinje, pachitsime ndi m’makhwawa.

-Kuteteza madzi a pa chitsime.

Kasungidwe ka madzi koyenera

-Kukumba madamu

-Kugwiritsa ntchito madzi amene tagwiritsira kale ntchito pothirira mbewu.

●Ngati tisunga madzi m'dera lathu. Anthu sadzasowa madzi akumwa, osamba ndi othirira mbewu.

MUTU 7: CHIWERENGERO CHA ANTHU OPEZEKA M'DERA LA MFUMU YAMPANDO

Anthu opezeka m'dera la mfumu yampando

-Amwenye

-Makaladi

-Anthu akuda

-Azungu

●Mu madera ena kuli kusakanikirana kwa mitundu ya anthu monga Alomwe, Achewa, Ayao, Angoni, Atumbuka, Asena, Atonga ndi Ankhonde.

Kufunika kodziwa chiwerengero cha anthu m'dera la mfumu yampando

-Kumathandiza boma pamene likukonza za chitukuko. Boma limaganiza za momwe lingaperekere ntchito zachitukuko monga sukulu, zipatala, miseu ndi misika m'madera osiyanasiyana

●Ntchito za chitukuko zimaperekedwa malingana ndi momwe chiwerengero cha anthu chilili m'deralo. Nthawi zambiri, chitukuko chimapita kumadera komwe kuli anthu ambiri.

Kusiyana kwa kachulukidwe ka anthu m'madera amfumu yampando

●Ku Madera kumene kuli mapiri, nkhalango zosungirako nyama zam'tchire, ndi nkhalango zotetezedwa anthu amakhala ochepa.

●Mu Madera monga ku zithaphwi, madambo ndi kumene kuli nthaka yopanda chonde, anthu sakhalako.

●Ku zigwa ndi ku zidikha kumene kuli nthaka yabwino anthu ambiri amathamangirako.

●M'matauni ndi m'mizinda anthu amachuluka chifukwa chopita kukafuna ntchito.

●Ku malo amchenga kopanda nthaka kumakhala anthu ochepa kwambiri.

MUTU 8: NJIRA ZOPEZERA NDALAMA M'DERA LA MFUMU YAMPANDO

Njira zopezera ndalama

-Usodzi ndi kugulitsa nsomba.

-Kugulitsa kaunjika.

-Kulima

-Kugwira maganyu osiyanasiyana

Kafalikidwe ka ntchito zopezera ndalama m'dera la mfumu yampando

-M'matauni ndi m'mizinda, anthu ambiri amagwira ntchito zopezera ndalama monga kukhala ndi masitolo, kugulitsa kaunjika, kugulitsa zakudya zosiyanasiyana ndi zamasamba, kugulitsa nsomba, nkhuku ndi nyama.

-Ku madera akumudzi, anthu amasowa chuma choyambira bizinezi. Anthu akumudzi amapeza ndalama pogulitsa nsomba, mbeu zakumunda ndi mbeu zamasamba. Enanso amagwira ganyu kuti apeze ndalama.

MUTU 9: ZAKUDYA ZOLIMA M'DERA LA MFUMU YAMPANDO

Zakudya zolima m'dera la mfumu yampando

-Chimanga

-Chinangwa

-Mapira

-Mpunga

-Soya

-Mtedza

-Nthochi

Kasungidwe ka zakudya zomwe timalima

a) Njira za makolo

-Kuumitsa ndi dzuwa kwambiri

-Kufutsa

-Kuthira phulusa

-Kuika mu chikwatu

b) Njira zamakono

-Kusunga m'filiji.

-Kusunga m'thumba.

Kufunikira kosunga chakudya mosamala

-Chakudya sichionongeka ndipo chimadzadyedwa komanso kugulitsidwa patsogolo.

MUTU 10: ZIKWANGWANI ZA PAMSEWU

Zikwangwani za pamsewu

-Ndi zizindikiro zomwe zimachenjeza, kufotokozera zoyenera kuchita ndi kusonyeza anthu oyenda pamsewu zomwe angakumane nazo patsogolo pawo, pofuna kupewa ngozi zapamsewu.

Mitundu ya zikwangwani

a) Zikwangwani zochenjeza

-Gulu ili ndi la zikwangwani zomwe zimatiwunikira kapena kutichenjeza kuti kutsogolo komwe tikupita kuli choopsa. Zikwangwani zimenezi zimakhala ndi mizere yofiira yangodya zitatu ndi mawu kapena chithunzi m'kati kapena kunja kwake, kufotokozera choopsa chomwe chili patsogolo pathu.

b) Zikwangwani zofotokozera zoyenera kuchita

-Izi ndi zikwangwani zomwe zimatilamula zoyenera kuchita pamsewu. Zikwangwanizi zimakhala ndi zilembo zozungulira zofiira ndipo m'kati mwa zilembomo mumakhala zizindikiro kapena mawu otifotokozera zoyenera kuchita.

c) Zikwangwani zopereka uthenga wapansewu

-Izi ndi zikwangwani zofotokozera anthu uthenga wapamsewu monga: dzina la malo, mtsinje, sukulu, chipatala ndi mtundu wamalowo.

Kufunika Kwa zikwangwani za pamsewu

●Zimathandiza kuchepetsa ngozi zapamsewu.

●Zimathandiza kufotokozera anthu zoyenera kuchita pamsewu.

Njira zosamalira zikwangwani zapamsewu

●Osachotsa zikwangawani munsewu.

●Osaphwanya zikwangwani zamunsewu.

MUTU 11: UFULU NDI UDONDO

Ufulu ndi udindo

Ufulu wa anthu m'dera la mfumu yampando

-Ufulu wokhala ndi zinthu.

-Ufulu wokhala ndi zinthu zamasewero.

-Ufulu wokhala ndi madzi abwino.

-Ufulu wokhala ndi zinthu zaumoyo.

-Ufulu wa malo abwino okhala.

-Ufulu wachipembedzo.

-Ufulu wakavalidwe.

Maudindo a anthu m'dera la mfumu yampando

-Makolo ayenera kusamala ana powapatsa zakudya, zovala ndi malo ogona komanso kuwatumiza kusukulu.

-Mabanja akuyenera kusamala odwala awo komanso kuthandizana mu nthawi ya mavuto ndi mtendere.

-Anthu onse ayenera kusamala zinthu za chilengedwe za m'dera lawo.

Udindo wa ana asukulu

-Kusamenya anzawo.

-Kuteteza ena pa nthawi yamavuto.

-Osatukwana ena.

-Kusamala malo onse asukulu.

Kufunika Kwa ufulu ndi udindo

-Aliyense amayembekezeka kuyang'anira zachilengedwe za m'dera lawo.

-Aliyense amasangalala ndi moyo wabwino.

-Aliyense amakhala wotetezedwa.

-Maganizo a aliyense amamveka.

-Anthu amadalirana ndi kuthandizana.

-Pamakhala umodzi pakati pa anthu.

MUTU 12: MITUNDU YA ANTHU M'DERA LA MFUMU YAMPANDO

Mitundu ya anthu m'dera

-Achewa

-Ayao

-Atumbuka

-Asena

-Alomwe

-Atonga

Zifukwa zimene anthu amasamukira ku madera ena

●Maukwati

●Nkhondo

●Kufuna malo odyetsera ziweto

Madera komwe kudachokera anthu osiyanasiyana

-Mozambique

-Democratic Republic of Congo (DRC).

-Tanzania

-South Africa

MUTU 13: CHIKHALIDWE CHA ANTHU M'DERA LA MFUMU YAMPANDO

Chikhalidwe cha anthu m'dera

-Chikhalidwe ndi chinthu chomwe anthu am'dera lililonse amatengera kuchokera kumakolo. Choncho anthu am'dera lililonse ali ndi udindo wosunga ndi kupititsa patsogolo chikhalidwecho ndi cholinga chosonyeza luso lawo losiyanasiyana.

Njira zosonyezera chikhalidwe

a) Chikhalidwe chopezeka m'zoyankhula

-Chikhalidwe ichi ndi chomwe anthu amachisonyeza poyankhula. Mwachitsanzo ponena nthano, kukamba miyambi, zining'a, ntchedzero, ndakatulo, mawu ndi mayina.

b) Chikhalidwe chopezeka m'nyimbo

-Chikhalidwe ichi ndi chomwe anthu amasonyeza poyimba nyimbo kapena kugwiritsa ntchito zing'wenyeng'wenye.

c) Chikhalidwe chopezeka m'ntchito zamanja

-Chikhalidwe ichi ndi chomwe anthu amasonyeza m'njira zingapo. Anthu amaumba mbiya, kusema zidole, mitondo, kuluka madengu, mphasa ndi kukongoletsa malo ndi utoto.

d) Chikhalidwe chopezeka m'masewero

-Chikhalidwe ichi ndi chomwe anthu amasonyeza pochita zinthu zosiyanasiyana monga kuvina magule, kuchita masewero osiyanasiyana ndi potsata miyambi ina.

Kufunika kwa chikhalidwe

-Kusangalatsa

-Kuphunzitsa

-Kupitiriza chikhalidwe chamakolo.

MUTU 14: MTOKOMA

Njira zamtokoma

a) Maliwu

-Iyi ndi njira yodziwika kwambiri. Imagwiritsa ntchito telefoni, wailesi, kanema, ng'oma kapena kuyankhulana.

b) Zolembedwa

-Njira iyi imagwiritsidwa ntchito m'zinthu monga kalata, mabuku, nyuzipepala, magazini ndi zikwangwani zapamsewu.

c) Makina amtokoma

-Iyi ndi njira yamakono, imagwiritsa ntchito zinthu monga telefoni, wayilesi, kanema ndi kompyuta, Njira imeneyi imadalira kwambiri magetsi.

Ntchito za mtokoma

-Kutumiza ndi kulandira uthenga.

-Ndi njira imodzi yosangalatsira anthu

-Imathandiza pa maphunziro

Njira zoonetsetsa kuti mtokoma ukugwira ntchito yake moyenera

●Njira zake zizipezeka mosavuta.

●Anthu azitsata ufulu wachibadwidwe.

●Anthu azikhala opirira

Ubwino wake wa mtokoma

●Siuvuta pogwiritsa ntchito.

●Mtokoma wina siufuna ndalama zambiri.

●Nthawi zina ndiodalirika.

●Nthawi zina umagwira ntchito mofulumira.

Kuipa kwake Kwa mtokoma

●Siumadalirika nthawi zina.

●Njira zina za mtokoma zimafuna ndalama zambiri.

●Nthawi zina umagwira ntchito mochedwa.

Mabungwe ndi anthu ena omwe amapereka njira zamtokoma

-Eni nyumba zoimbiramo telefoni.

-Positi ofesi.

-Eni nyumba zakompyuta.

-Eni nyumba zoonetseramo kanema

-Nyumba zowerengeramo mabuku.

-Eni wailesi.

-Eni ng'oma.

Udindo wa anthu posamalira katundu wa mtokoma

-Kusamalira bwino katundu yense wa mtokoma monga nthambo zamagetsi ndi telefoni, mapositi ofesi, nyumba zowerengera mabuku, misewu, njanji, milatho ndi zikwangwani zapamsewu.

MUTU 15: MTENGATENGA

Njira za mtengatenga

●Kugwiritsa ntchito njinga yamoto.

●Kugwiritsa ntchito sitima yapamtunda ndi yapamadzi.

●Kugwiritsa ntchito ndege.

Zinthu zofunikira pa ntchito za mtengatenga

●Misewu

●Njanje

●Mabwalo andege

●Nyanja

●Mitsinje

Mabungwe ndi anthu ena omwe amapereka njira zamtengatenga m'dera

-Mabasi

-Maminibasi

-Ngolo

-Njinga

Ubwino wosamalira za mtengatenga

●Zimathandiza kupewa ngozi.

●Zimathandiza kupita ku malo osiyanasiyana.

BUKU LOMWE LAGWIRITSIDWA NTCHITO

●Buku la Ophunzira la Social Studies la Sitandade 4

ULEMU NDI MATAMANDO ZIPITE KWA MULUNGU!!!!!!!!!!!!!!!